

OPANDA NDALAMA KAPENA

OPANDA MTENGO



Ndithudi ndi chamwayi kubwerera ku kachisi, mmawa uno. Ine ndikungodabwa . . . M'bale Neville ananena kuti ambiri samatha kumva kumbuyoko. Mukundimva ine bwino lomwe tsopano, kumbuyo uko? Kodi zonse ziri bwino? Chabwino. Ndine—ndine wamng'ono, chotero ndimayenera kupanga phokoso lambiri kuti anthu adziwe kuti ndiripo.

² Chotero, ine ndikukumbukira nthawi ina pamene ine ndinkagwira ntchito Kolipirira Mabilu. Ine ndikamakwera pa sitepe. . . Ndipo ine ndinkakonda kuvala nsapato zazikulu kwambiri, zokhala ndi gogoda pa izo, kuchokera koyendera nthambo za m'mwamba. Ndipo ine ndinkabwera chokwera masitepe. Ndipo Akazi a Ehalt, yemwe ali mzanga wa ine, amakhala pa switchibodi. Ine ndikutsimikiza Bambo Ginther kumeneko akhoza kumuzindikira iye, bwino lomwe. Chotero Edith anati, “Billy, iwe umapanga phokoso lowonjeza, losagwirizana ndi munthu wamng'ono, yemwe ine ndinayamba ndamuwonapo.” Ndikuponda magogoda awa aakulu, ndikukwera pamwamba pa masitepe.

³ Ine ndinati, “Chabwino, Edith, ndine wamng'ono kwambiri, ine ndiyenera kuyesetsa kuti aliyense adziwe kuti ine ndiripo, pomapanga phokoso lambiri.”

⁴ Chabwino, ine ndinangopita mkati kuti ndikaimbe. M'bale Neville anali atandiuza ine kuti bwenzi lathu labwino, M'bale Roy Roberson, monga ali kutali ndi msonkhano mmawa uno, pa chifukwa chakuti akudwala. Lake. . . Iye wakhala ali ndi dzino lophatana. Ilo layambitsa matenda, ndipo zikumpatsa iye kutentha thupi. Ndipo iye ndiwoti akalizulitse ilo, ine ndikuganiza, pomwepo. Ndipo Roy wakhala ali ngati bambo kwa ife kuno, ndipo ife timamukonda iye. Ndipo ine ndinati, “M'bale Roy, ine—ine ndikukalowa tsopano, mu maminiti pang'ono chabe, mu msonkhano.” Ine ndinati, “Ine ndikaupempha mpingo kuti ife tonse tikupempherere iwe, mmawa uno,” ndipo mawa pamene iye azidzapita uko, kuti akasamalire izi. Dzinolo latuluka mopingasa, kapena chinachake, laphatirira molakwika, ndipo iwo akuyenera kuti akalidulepo ilo, ndi kulichotsapo.

⁵ M'bale Roy ndi wa nkhondo wakale, monga inu nonse mukudziwa, kuchokera ku Nkhondo Yachiwiri ya Dziko lonse, yemwe anawomberedwa m'zidutswa. Ndipo kukanakhala kuti si kwa ubwino wa Mulungu, iye sibwenzi ali moyo nkomwe.

Iye anakagonekedwa pamodzi ndi akufa, kwa nthawi yaitali; manja ataomberedwa kuno, ndipo miyendo itaphulitsidwa, ndipo mitsempha yaikulu yonse itaphedwa. Ndipo adokotala anati, “Ngati iye angakhale moyo konse, iye sadzayenda sitepe nkomwe.” Mwa chisomo cha Mulungu, iye amagwira ntchito tsiku lirilonse, kumakwera ndi chirichonse. Mulungu wakhala ali wabwino kwa iye chifukwa iye ndi munthu wabwino, ndipo ife timamukonda iye. Ndipo ife, ife tiri—ife sitiri tonse. . .

⁶ Ife tikamakhala moyo wabwino, izo sizitanthauza kuti ife ndiwoti sitingakumane ndi mavuto. Moonamtima, izo zimatanthauza kuti mavuto onse alunjikitsidwira njira yathu. “Pakuti zambiri ndi zotunduzwa za olungama, koma Mulungu amamuwombola iye kwa izo zonse.” Ndiro gawo la ulemelero.

⁷ Chotero ife tingopempha pemphero lapadera mmawa uno, la M’bale Roy. Ine ndikudabwa ngati alipo aliyense muno, pakalipano, akufuna kuti apemphereredwe, akufuna kuti akumbukiridwe mu mawu a pemphero? Ngati iwo angakweze chabe manja awo. Chabwino. Ndizo zabwino. Tiyeni tingoima kwa kamphindi chabe, ngati inu mungatero, pamene ife tikupemphera.

⁸ Ambuye, ife tikubwera lero, pakuyamba kwa sabata. Ndipo dzuwa likungotenga njira yake tsopano, kuti liwuluke kudutsa pa dziko lapansi, kuti libweretse kuwala ndi moyo kwa zinthu izo zimene ilo linakonzedwera kuti lidzachite. Ndipo pa kuyamba kwa msonkhano umene. . . Ife tiri gawo la Mpingo Wanu, umene wayitanidwa kuti udzachititse misonkhano ya machiritso, machiritso a thupi; kukakwaniritsa zofuna ndi zokhumba za Ambuye wathu wodala Yemwe anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa. Ndipo ife tikufuna tipemphe, pa kuyamba kwa msonkhano, pamene ukuyamba kutenga mapiko ake, mu nyimbo, ndipo mitima yathu ikuyamba kukwezedwa m’mwamba, kuti ife tikhoze kukumbukira, mmawa uno, Ambuye, m’bale wathu wokonedwa, wofunika, Roy Roberson, wantchito Wanu wodzichepetsa. Ndipo ife tikudziwa kuti Inu munasunga moyo wake ku bwalo la nkondo, ndipo Inu mwakhala muli wabwino kwa iye. Ndipo lero iye akuzunzika ndi kutunduzidwa, mwakuti iye sanathe kubwera ku tchalitchi.

⁹ Ndipo, Ambuye, pamene iwo anali kupemphera mu nyumba ya Yohane Marko, kunali Mngelo anatsika kudzalowa mnyumba ya ndende, kumene Petro anali mu msinga, kumeneko anatsigula zitseko, mozizwitsa, ndipo anamutsogolera iye kutuluka panja.

¹⁰ O Ambuye, Inu mukadali panobe Mulungu. Angelo amenewo ali pa kutuma Kwanu mmawa uno. Ife tikupemphera, Ambuye, kuti pamene ife tikupemphera kuno mnyumba ya Mulungu, kuti Angelo atsikire ku nyumba ya M’bale Roberson. Khumbo lake ndi kukhala pamalo ake kuno, koma chosautsa chamugwirira

iyе pansi. Ndipo mulole Angelo a Mulungu amuwombole iye, amupange iye akhale bwino, kuti akhoze kudzatenganso malo ake ku nyumba ya Mulungu.

¹¹ Alipo ena omwe abwera kudutsa movuta, iwo—iwo akhala akudwala. Ndipo ife tamuwona mkazi wachikulire, pamene iye anali pafupi kuti akhale pa mpando wake, akukweza manja ake, pamene iye amatsimphina pa mapazi ake. Iye wabwera ku nyumba ya Mulungu, kuti adzachiritsidwe. Perekani, Ambuye, kuti iye apite akuyenda, wanthete ndi chitsikana cha mkazi wamng’ono.

¹² Ena onse amene anakweza manja awo, ambiri a iwo anakwera, chifukwa kwalembedwa, ndipo zinawerengedwapo mobwereza, “Zochuluka ndi zotunduza za olungama.” Mulole ife tiulukire kutali lero mu chikhulupiriro, mikono ya chikhulupiriro, imene imatiwombola ife kutichotsa ku nthenda ndi zotunduza zonse. Pamene msonkhano watha, pasakhale wina wofooka pakati pathu.

¹³ Perekani, Ambuye, kuti wosakhulupirira aliyense akhale wokhulupirira. Ndipo pamene ife tikusinkhasinkha pa Mawu Anu, mulole Mzimu Woyera uwatenge Iwo ndipo uwaike Iwo mmitima yathu, ndipo m’menemo uziwathirira Iwo kufikira Iwo asandulike chipatso cha Mawu. Tichitireni ife ichi, Ambuye, pamene ife tikuweramitsa mitu yathu modzichepetsa ndi kupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

Inu mukhoza kukhala.

¹⁴ Tisanalowe mu uthenga wa msonkhanowu mmawa uno, ine ndikufuna kuika pa malingaliro anu, moyandikira pang’ono. Ngati pali aliyense wa inu amene ali ndi matchuthi, ndipo akufuna kudzakhala nawo pa umodzi wa misokhano imene ikachitikire mu Middletown, Ohio, kuyambira Lolemba, sabata, iwo udzakakhala pa mabwalo a misasa.

¹⁵ Kodi inu mukulidziwa dzina la mabwalo amisasawo, Gene? [M’bale Gene akuti, “Anati kunali thwelofu mailosi kunja kwa Middletown.”—Mkonzi.] M’bale Sullivan. Middletown ndi mzinda waung’ono, ine ndikuganiza pafupifupi ngati Jeffersonville kuno. Ndi kuchimake kwa basiketibolo. M’bale Sullivan ndi m’busa kumeneko. Uliwonse wa mipingo ya Full Gospel, yomwe kuli sikisite chakuti ina yomwe ikuthandizira mu msonkhano uwu, adzakhoza kukuuzani inu kumene mabwalo amisasi ali.

¹⁶ Ndipo kukakhala malo ogona ambiri ku mabwalo a misasako, ine ndauzidwa chomwecho, kuti akasamalire anthu omwe akufuna kubwera. Ndipo misonkhano idzayamba Lolemba kudutsa mpaka Loweruka, masiku sikisi. Ndipo siidzakhlapo Lamlungu, chifukwa cha matchalitchi ena, kuti iwo akhoza kudzapita ndi kukhala ndi misonkhano yawo

ya nthawizonse. Mwinamwake, kudzakhala misonkhano ya machiritso, kapena pemphero la odwala, usiku uliwonse. Ndipo aliyense akuitanidwa. Ndipo iyo idzayamba pa Ogasiti 10, mpaka pa 15, Lolemba kudutsa mpaka Loweruka. Ndipo ngati inu muli ndi tchuthi, ndipo—ndipo tchuthi chanu chikubwera, ndipo inu mungafune kukhala nacho mwanjira imeneyo, chabwino, ife ndithudi tidzakondwa kukhala nanu.

¹⁷ Ine ndikufuna ndiwalimbikitsenso onse iwo amene sanabatizidwe mu ubatizo wa Chikhristu, kuti atsalire mmawa uno ndipo aziganizire izo. Ndi kumakonzekera utumiki wa ubatizo umene utsatirepo mu pafupifupi maminiti forte faivi tsopano, ine ndikuganiza. Izo zidzakhala pano pa tchalitchi.

¹⁸ Ife kwambiri tiri poti tiziwalimbikitsa anthu kuti azibatizidwa mu ubatizo wa Chikhristu, podziwa kuti uwo ndi wofunikira ku chipulumutso. Pakuti kunalembedwa ndi Ambuye wathu, kutuma Kwake komaliza, kutuma Kwake komaliza kwa Mpingo. Kapena, pamene Iye ankawutuma Mpingo, kumapeto, Iye anati, “Pitani mu dziko lonse, ndipo kalalikireni Uthenga kwa cholengedwa chirichonse. Iye amene akhulupirira nabatizidwa adzapulumutsidwa.” Chotero ife tikudziwa kuti ndi zofunikira kuti ife tizibatizidwa mwa kumizidwa.

¹⁹ Ndipo ife tikhala osangalala kuchita ntchito iyi kwa inu, kwa aliyense yemwe watsimikiza mu mtima mwawo kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu, kuti Iye anafa kuti adzapulumutse ochimwa, ndipo inu ndi amene Iye anafa kuti adzakupulumutseni; ndipo mukufuna kubwera ndi kudzabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anu; kunena, kwa dziko lapansi, kuti inu mukukhulupirira kuti machimo anu achotsedwa, ndi kuti inu tsopano mukupita kukakhala wophunzira wa Ambuye Yesu, kuti mukatenge maimidwe anu.

²⁰ Ngati inu mulibe tchalitchi choti muzipitako, ife tidzakhala okondwa kukhala nanu mu chiyanjano ndi ife. Ife tiribe umembala kuno. Ndi kachisi wotseguka, kwa Thupi lonse la Khristu, la chipembedzo chirichonse. Ife timaima ngati chipembedzo cha onse. Ndipo ife timatsegula makomo kwa anthu onse, posawerengera omwe iwo ali, mtundu, fuko, kapena kachikhulupiriro, aliyense ndi wolandidridwa. “Aliyense yemwe akufuna, bwerani.” Ndipo ngati inu mulibe mpingo wina uliwonse, ife tidzakhala okondwa kuti inu mungobwera ndi kudzayanjana nafe. Palibe chirichonse choti nkujowina. Mudzangobwera mkati muno pamene makomo atsegulidwa, ndi kudzayanjana nafe. Ndizo zonse zimene inu mukusowa; mungobwera monga chomwecho. Mubwere ndi mtima wotseguka, mudzaike mapewa anu pa gudumu, ndipo mutithandize ife pamene tikukanikizira patsogolo pa chifukwa cha Ufumu wa Mulungu. Pakuti, ife tikukhulupirira kuti

oralo, posachedwapa liyandikira, limene zinthu zonse zimene zinayankhulidwa mu Baibulo zidzakwaniritsidwa.

²¹ Nzosakayikitsa kuti ambiri a inu munawerenga za Khrushchev, maneno ake ku U.N., tsiku lina, monga zinabwerezedwa mowerenga kwa ine kuchokera mu pepala ya ku Canada, ndi mzanga. Iye anati, “Ngati kuli Mulungu, Iye ali wokonzeka kuti asese ndi kuyeretsapo kachisi kachiwiri, ndi inu achikapitolisiti, monga Iye anachitira pachiyambi.” Chotero tsopano inu mukhoza kuwerenga pakati pa mizere, “Iye ali wokonzeka kuti asese kachisi kachiwiri.” Ndipo ngoipa, wachikominisiti angati anene chinthu ngati chimenecho? Iye anali ndi chinachake, ngakhalebe. Uko nkulondola. Anali achikapitolisiti, poyamba, amene anayambitsa vuto. Ife ndife achikapitolisiti.

²² Ine ndinamumva m’busa wathu wokondedwa, wapamtima, M’bale Neville, akunena ndemanga pa televizioni yake... kapena pa kulengeza kwa pa wailesi, mmawa wina, zimene zimangobwerabwera, m’malingaliro anga. Ine sindikutha kuiwala basi zimenezo. Ine ndinazibwereza izo kwa bwenzi la ine, usiku wapitawu. Ndipo izo zinani izi, kuti kudzakhala... Mzimu Woyera ukadzati wachotsedwa, kuchoka pa dziko lapansi, kuti chipembedzo chofunda cha tchalitchi chizidzapitirirabe, osadziwa kusiyana kwake. Kodi inu munayamba, mwateropo... Ndi angati anamva zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi izo sizinali zododometsa? Iwo sakuwudziwa Mzimu Woyera, chotero iwo sadzadziwa pamene Iwo wapita, ndipo iwo adzakhala akungopitirirabe chimodzimodzi momwemo. Pamene wotsirizayo adzasindikizidwe kulowa mu Thupi la Khristu, iwo adzakhala akupitirirabe, kuyesetsa kuti abweretse owatembenuza kwa Iwo, chifukwa iwo sakudziwa chomwe Iwo uli. Ndipo zipembedzo zawo zofunda zizidzapitirirabe chimodzimodzi monga iwo anali. Tsopano, izo zikhoza kusazimirira mwa inu monga izo zinachitira kwa ine, koma ilo kwenikweni linali neno lododometsa. Kutu, iwo adzakhala kutali kwambiri zedi, basi mu miyambo ya chipembedzo, kufikira kuti iwo sadzawusowa Mzimu Woyera, chifukwa iwo sakudziwa chomwe Iwo uli, kuyamba ndi kuyamba.

²³ Mulungu atichitire ife chifundo. M’bale, ine ndikufuna kukhala mmoyo uno, ndicho chokhumba changa, kufikira kuti ngakhale kachidutswa kakang’ono ka kukhumudwa Kwake, ine ndizikadziwa iko mu mtima mwanga. Ine nditachita chinachake chimene chingamukhumudwitse Iye, ine ndizitha kuchimverera icho mu kamphindi chabe.

²⁴ Ndiye munene, zakuti Iyeyo kulibeko; ine sindikufuna kuti ndidzakhale kuno pamene Iye adzakhale kulibeko. Ine ndikufuna ndidzakhale nditapita pamenepo, inde, bwana, chifukwa sipadzakhala Magazi pa mpando wachifundo. Iko

kudzakhala kwa mdima ndi kwa utsi ndi kwakuda. Malo oyera sadzakhala ndi Woimirira mlandu kumeneko, kuti achonderere mlandu wathu pa nthawi imeneyo. Inu mukudziwa Lemba limanena zimenezo? Malo oyera amachita utsi. Panalibe Magazi pa mpando wachifundo, kenako ndi chiweruzo.

²⁵ Ngati Ambuye, nthawi ina molawirira chirimwe chino, adzatipatsa ife chitsitsimutso cha mausiku angapo. Ine ndinangopanga izo mmalingaliro anga, ine ndikufuna kuti ndidzatenge Bukhu lija la Chivumbulutso, ngati phunziro pa izo, kudzangodutsa Bukhu ilo la Chivumbulutso, pa.

²⁶ Tsopano, lero, ine ndikudziwa kuti alipo ambiri abwera, kuti adzapemphereredwe. Ndipo ofesi yanga inali yotseka lero, kapena sabata ino. Ndipo anthu ena anali atabwera, sanapeze mwayi woti apemphereredwe, kunja uko, chifukwa chakuti anyamata anali atapita, kwa tsiku kapena chomwecho, kuti akapume. Iwo ali ndi ntchito yambiri yoti achite; ntchito yawoyawo, kuphatikiza ntchito ya pa kachisi, ndi kuimba kwa foni yanga ndi chirichonse. Izo posakhalitsa zimakufikira mmisempha mwako. Ndipo chotero ndiye ndicho chifukwa chake. Ine ndikudziwa ine ndimayenera kupita kwinakwake, kamodzi mu kanthawi, ndi kukachita chinachake chosiyana, ndipo ine ndikudziwa iwo amatero, nawonso. Chotero, iwo anandiyimbira ine. Ine ndinati, “Ine ndikuganiza izo zikhala bwino.” Ndipo ife tipempherera odwala, mu mphindi zingapo.

²⁷ Ndipo ine ndinaganiza ife tiwerenge zina kuchokera ku Mawu a Mulungu. Ngati inu muli ndi Baibulo lanu tsopano, tiyeni titembuzire ku Bukhu la Yesaya. Ine ndimakonda kukuwonani inu mukutenga Bukhu lanu ndi kuliwerenga Ilo. Ine ndikuwerenga. . . Ngati inu si Mawu oposerera amodzi chabe kapena awiri ife tiwerenga, apobe, ndi Mawu Amuyaya, Achisavundi a Mulungu. Iwo sangathe kupita. Mutu wa 55 wa Yesaya, phunziro, “Chipulumutso chosatha.”

Ho, aliyense amene ali ndi ludzu, bwerani inu kumadzi, ndipo iye amene alibe ndalama; bwerani inu, mudzagule, ndi kudya; eya, bwerani, mudzagule vinyo. . . mkaka opanda ndalama ndi opanda mtengo.

Bwanji inu mukutaya ndalama pa izo zimene siziri chakudya? ndipo mukugwirira ntchito chimene chiri chosakhutitsa? mvetserani mwachangu kwa ine, ndipo mudyane inu izo zimene ziri zabwino, ndipo mulole moyo wanu ukondwere wokha mu kunenepa.

Tcherani khutu lanu, ndipo mubwere kwa ine: imvani, ndipo moyo wanu udzakhala moyo; ndipo Ine ndidzapanga pangano losatha ndi inu, ngakhale zifundo zotsimikizika za Davide.

28 Ine ndikufuna kuti ndiyankhule ndi inu, kwa mphindi pang'ono chabe, pa phunziro: *Opanda Ndalama Kapena Opanda Mtengo*.

29 Kuli zinthu zosangalatsa zochuluka kwambiri za masiku athu. Kuli zochuluka kwambiri zikukopa anthu ku zimene ife tingazitchule “zosangalatsa,” ndipo ndi za anthu onse, amisinkhu yonse.

30 Kuli zokopa za achinyamata, magule amakono ndi maphwando a gwedemula, ndi nyimbo zimene iwo alinazo zimene zimapita ndi izo. Ndipo zonsezo ndi zokopa, za chisangalalo.

31 Ine sindikusamala kaya khomolo ndi labwino chotani limene mwanayo waleredweramo, ndi momwe iye waphunzitsidwira kuchita bwino; ngati mwana ameneyo sanalandire chomuchitikira cha Kubadwa kwatsopano, nyimbo za gwedemula zingagwire tcheru chake mwamsanga basi iye akangozimva izo. Chifukwa, mwa iye, munabadwa mwa iye, mwa chirengedwe, mzimu wachithupithupi. Ndipo mphamvu ya mdierekezi ndi yaikulu kwambiri, lero, mpaka imagwira mzimu uwo wa wamng'ono uyo.

32 Ndipo ndi mochuluka motani izo zingachite kwa wamkulu, ndiye, yemwe wakana Kubadwa kwatsopano! Chifukwa, pokhapokha ngati moyo wako wasinthika, ndipo iwe watembenuka ndipo wabadwa mwatsopano, kulowa mu Ufumu wa Mulungu, chikhalidwe chako chikhalabe cha zinthu za dziko lapansi, ziribe kanthu kuti ndiwe wachipembedzo bwanji, pokhapokha ngati chimenecho chasinthidwa mwa iwe. Iwe ukhoza kumapembedza ndi kukhala wachipembedzo, komabe icho chidzakhala ndi mtundu wina wa mphamvu yokoka kwa iwe, chifukwa munthu wakale uyu wa tchimo ndi zokhumba zake sanafebe mwa iwe.

33 Koma pamene umulola Khristu akhale pa mpando wachifumu mu mtima mwako, zinthu zimenezo sizimavutanso. Izo ndi zazikulupo kwambiri.

34 Ine sindingathe kutchula dzina la munthuyo, chifukwa ine sindingathe kulingalira za dzina lake tsopano, koma ambiri a inu mumukumbukira iye. Iwo amati kunali chilumba kumene amuna amapitako, mwa uchifwamba, ndipo akazi amatulukirako, akuyimba. Ndipo nyimbo zawo zimakhala zodolola kwambiri, mwakuti oyenda pamadzi akamadutsa, pa ngalawa, amakhoza kupitako. Ndipo kenako asilikari achifwambawo amakhoza—amakhoza kuwagwira oyenda apamadzi awa mowadzidzimutsa, ndi kuwapha iwo. Ndipo mwamuna wina wamkulu ankafuna kuti adutseko. Ndipo iye anawauza oyenda pamadzi ake kuti amumangirire iye ku chintengo cha chinsalu cha mu sitimayo, ndi—ndi—ndi kuika chinachake mkamwa mwake, kuti iye asathe kufuula; ndi—

ndi kuika zotseka m'makutu a oyenda pamadzi ake, kuti iwo asakhoze kumva, ndi kumayenda akudutsa, kuti amve izo. Ndipo akaziwo anatulukira, akuvina ndi—ndi kumafuula, ndi kumaimba, ndipo, oh, izo zinali zopambana kwambiri, mpaka iye anazisupula khungu la mikono yake, akufuula kwa omuyendetsa ake, “Khotani! Khotani!” Koma iwo samamumva iye, anali atatsekera mmakutu mwawo.

³⁵ Ndiyeno iye anayenda kupita ku malo ena kumene iwo anali kuti amuchotse iye, kapena, amasule manja ake, ndipo iye anali kuti achotse zotsekera mmakutu awo. Kumeneko, pamene amayenda pa msewu, iye anamva woyimba amene anali wapamwamba kwambiri kuposa ajawa uko, kuti pamene iye amadutsanso, iwo anati, “Oh, woyendayenda wamkulu, kodi ife tikumangirireninso inu ku mtengo kachiwiri?”

³⁶ Iye anati, “Ayi, ingondimasulani ine. Ine ndamva chinachake chopambana kwambiri zedi, kufikira kuti izo sizidzandivutitsanso ine nkomwe.”

³⁷ Ndi mmene izo zimakhalira ndi Mkristu wobadwa-kachiwiri. Iwo anapeza chinachake chopambana kwambiri kuposa gwedemula ndi zisangalalo za mdziko lino. Iwo amasangalatsidwa ndi Mzimu Woyera. Iwo ndi wopambana kwambiri zedi, kufikira kuti dziko ndi lakufa kwa iwo.

³⁸ Koma pamene inu mupita ku zisangalalo zotchipa izi, inu mukuyenera kukumbukira kuti inu mumayenera kutenga ndalama zochulukika. Mnyamata wamng'ono yemwe amatengera chibwenzi chake chachikazi ku maphwando awa ndi magule awa, ndi zina zotero, akalipira zochulukika kwambiri za malipiro ake a pa sabata. Ndipo anthu achikulire amene amayesera kupeza chisangalalo popita ku mabwalo a mowa, kuti akamwe kuchotsa nkhawa zawo za msabata, iwo amayenera kuti akalipire ndalama zambiri. Ndipo kodi iwo amapezako chiyani kwa izo? Iwo sapezako chirichonse koma kupweteka kwa mtima.

³⁹ Ndipo kumbukirani, inu mudzayenera kuti mudzakambirane ndi Mulungu tsiku lina pa izo. “Ndipo malipiro a tchimo ndi imfa.” Inu simupindula chirichonse kuno pa dziko lapansi, pochita zimenezo. Ndi kunyezimira kwabodza. Kumwa kumangowonjezera chisoni. Tchimo limangowonjezera imfa pa imfa. Potsirizira panu padzakhala kulekanitsidwa ndi Mulungu, Mwamuyaya, kukalowa mu Nyanja ya Moto. Ndipo inu simudzapindula chirichonse, koma mudzaluza.

⁴⁰ Ndiye Mulungu akubwera ndipo akufunsa funso, “Chifukwa chiyani iwe umataya ndalama zako pa zinthu izo zimene ziri zosakhutitsa? Chifukwa chiyani iwe umachita zimenezo?”

⁴¹ Ndi chiyani chimawapangitsa anthu kufuna kuchita zimenezo? Iwo amawononga zonse zimene iwo ali nazo, zonse zimene iwo angakhoze kuzigwirira ntchito, kuti akagule chakumwa, kuti akamuveke mkazi wina amene iwo amayenda

naye, kapena mtundu wina wa zosangalatsa za chidziko, chisiliro chamanyado.

⁴² Koma ife timazuidwa mu Baibulo, ndipo timafunsidwa kuti tibwere kwa Mulungu, “Ndipo kuti tidzagule chimwemwe Chamuyaya ndi Moyo Wamuyaya, opanda ndalama kapena opanda mtengo.”

⁴³ Zinthu zimenezo sizingakhoze kukhutitsa, ndipo mapeto a zimenezo ndi imfa Yamuyaya. Ndipo izo zimakuthera iwe ndalama zonse zimene iwe ukhoza kuzisonkhanitsa pamodzi, kuti ukhale chi—chikhwaya kapena msangalatsi, kapena mnyamata wanthabwala, kapena chirichonse chimene iwe ukhoza kukhala, kapena mtsikana wotchuka, kapena chirichonse chimene chiri. Izo zimakutengera iwe zonse zimene iwe ungazibweretse pamodzi, kuti uchite zimenezo. Kuvala mu mavalidwe apamwamba kwambiri, ndi—ndi kuchita zinthu zimene dziko limachita, basi nkuthela kukolola cheke cha chiwonongeko Chamuyaya.

⁴⁴ Mulungu anati, ndiye, “Chifukwa chiyani?” Kodi ife tidzachita chiyani pa Tsiku la Chiweruzo, pamene ife titi tidzafunsidwe chifukwa chomwe ife tinachitira zimenezo? Kodi yankho lathu lidzakhala chiyani? Kodi lidzakhala yankho lotani kwa Achimerika amakono, omwe amanena kuti iwo ali fuko la Chikhristu? Ndipo pali ndalama zochuluka zimene zimawonongedwera pa mowa, mu nthawi ya chaka, kuposa za chakudya. “Chifukwa chiyani mukuwonongera ndalama zanu pa zinthu za mtundu umenewo?” Komabe, boma likhoza kukutumizani inu ku ndende, chifukwa cha msonkho wa madolla asanu umene inu munatumiza mwinamwake ku bungwe lina limene silinaikidwe moyenera kuti lizilandira misonkho, potumiza wa misionare wina kutsidya kwa nyanja. Ife tidzakafunsidwa tsiku lina, “Chifukwa chiyani iwe unachita zimenezo?”

⁴⁵ Ife ndife fuko la Chikhristu, ndipo mabilioni akutumizidwa kwa anthu awo kumeneko, amene tikuyesera kuti tiwagule ubwanawe. Tsopano iwo akuzikana izo. Nzosadabwitsa Khrushchev anati, “Ngati kuli Mulungu, Iye asesya nyumba Yake yachifumu kenanso.” Achikunja akukhoza kupanga maneno oterowo, kuti abweretse manyazi pa ife. Ndi chinthu chamanyazi bwanji icho chiri! Ndipo ife tikumadzitchula tokha Akhristu.

⁴⁶ Mulungu anati, “Bwerani, mudzagule Moyo Wamuyaya, opanda ndalama, opanda mtengo.” Moyo, kuti mudzakhale moyo kwanthawi zonse, ndipo ife tikupotoletsa misana yathu kwa Iwo ndi kuseka pa nkhope Pake. Kodi ife tidzachita chiyani pa Tsiku limenelo? Kodi kudzakhala chiyani. . . ?

⁴⁷ Ngati Mulungu watipatsa ife zinthu zoti tichite, ndipo watipatsa ife ndalama, ndipo watipanga ife kukhala fuko lolemera kwambiri pansu pa miyamba, ndiye Mulungu

adzatifunsa kodi tinachita nazo chiyani zimenezo. Chifukwa chiyani ife timawonongera ndalama zathu pa zinthu zimene nzosakhutitsa? Osati kokha kwa fuko, koma izo zingakhale kwa munthu payekha payekha; kuchokera ku ndalama ya chitsulo, mpaka ku ma milioni a madolla, aliyense adzapatsidwa.

⁴⁸ Pamene azibambo anaphana wina ndi mzake: ine ndinawerenga nkhani posakhalitsapa, kumene anyamata awiri amagwira ntchito mu msasa wosaka. Mmodzi anali ndi ana asanu, winayo anali ndi awiri. Ndipo mmodzi wa iwo anali woti achotsedwe ntchito. Ndipo mmodzi wa anyamatawo yemwe anali ndi ana awiri, kapena anali ndi ana asanu, anamverera kuti iye amaifunitsitsa ntchitoyo kuposa iye amene anali ndi ana awiri; ndipo anapita kosaka ndi iye, ndipo anamuwombera iye ku nsana.

⁴⁹ Ndalama, ndiwo mtundu wa fuko, ndiwo mtundu wa kumverera, ndiwo mtundu wa mzimu umene ukuwalamulira anthu.

⁵⁰ Ndiye inu mukhoza kuwona ndikofunika bwanji momwe Kubadwa kwatsopano kukuyenera kukhalira. “Iwe uyenera kubadwanso kachiwiri.” Izo zikuyenera kutero. “Bwerani kwa Ine, ndipo mudzagule opanda ndalama.”

⁵¹ Inu simungati, “Ine ndinalibe ndalama.” Inu simukusowekeka ndalama iliyonse. Izo zikuperekedwa mwaulere.

⁵² Ife Achimerika tinazolowera kulipira njira yathu pa chirichonse. Ndiyo mbalume yathu. “Ife timalipira pa zinthu. Ife tiri ndi ndalama.” Timawonetsera mapepala a madolla athu ku maiko ena, ndi zina zotero, amene ali osauka. Ukamayenda, iwe umawona alendo akulowamo, onse atavala nthenga ndi zofewa. Achimerika amapita kwa iwo. Chinthu chimenecho ndi chisiliro chonyansa pamaso pa Mulungu. Zimenezo sizidzagula njira yathu ya Kumwamba. Koma chirichonse mu Amerika, ife timayenera kulipira njira yathu.

⁵³ Iwe ukapita ku malo odyera, ndipo iwe ukadya chakudya chamadzulo chako. Ndipo ngati iwe suyika ndalama pa tebulo, kumupatsa woperekeka ameneyo, pamakhala tsinya limene limabwera pa nkhope, pambuyo pakuti kampani yomwe iye akuigwirira ntchitoyo yamulipira. Ndipo izo zimayenera kukhala pafupifupi teni peresenti, kapena kuposerapo, ya bilu yakoyo. Ngati iwe sutero, woperekeka ameneyo amakuyang’anira iwe pansu ngati womana kapena winawake ngati wo—wowumira. Pamene, iye amalandira ndalama zake. Ine ndikuganiza ndi chitonzo ndi chamanyazi, kuchita zimenezo. Ine ndikuganiza ndi kuweruza kolakwika kwa fukoli. Kale anali, anthu abwino, malo abwino, samalola zimenezo. Koma zonsezo zikulowa mu mzimu umodzi waukulu.

54 Ine ndinali pa ulendo, pa sitima. Ndipo wolandira alendo . . . Ine ndinali ndi kachikwama kakang'ono mdzanja limodzi, ndi sutukesi kwinako, ndipo kabokosi ka zometera mkhwapa mwanga, ndipo ndimayenda. Wolandira alendo anabwerapo, anati, “Kodi ine ndingakunyamulireni inu zimenezo?”

55 Ine ndinati, “Oh, ine ndikungopita ku sitima uko, bwana. Zikomo inu, kwambiri zedi.” Basi pafupi, oh, mayadi sate.

56 Iye anati, “Ine ndinyamula izo,” ndipo iye anatenga chinthu chaching'onocho ndi kuchinyamula mmwamba icho, ndi kumayenda.

57 Chabwino, pamene iye anafika, ine ndinaganiza mwinamwake ine . . . ine ndimadziwa kuti iye amalipidwa, koma ine ndingomupatsa iye—ndimupatse iye theka la dolla. Iye mwinamwake ananyamula, katundu wangayo, kwa pafupifupi, mwina, miniti; pafupifupi kutalika kwake ngati kumapeto a kachisi uno, kumene iye anakapeza sitima. Ine ndinakwera mu sitimayo, poyamba, ndipo ndinangofikira pansu ndi kutenga izo. Ine ndinamupatsa iye theka la dolla.

Iye anati, “Miniti chabe!”

Ine ndinati, “Ndi chiyani, bwana?”

Iye anati, “Ine ndinakunyamulirani inu zikwama zitatu!”

Ine ndinati, “Inde, bwana, uko nkulondola. Ndiye, palakwika chiyani?”

58 Iye anati, “Mtengo wanga wotsikitsitsa ndi masenti twente faifi pa chikwama. Inu muli ndi twente faifi yanga inanso.”

Mukuona, chimenecho ndicho Chimerika, chirichonse chiyenera kulipiridwa.

59 Iwe ukapita koyenda mu galimoto yako ndipo iyo ikagwera mu dzenje, ndipo iwe ukampeza winawake kuti akukokere iwe pamtunda. Iwe uyenera kuti ukonzekere kulipira, chifukwa iwo akulipiritsa iwe chifukwa cha izo. Makako akabwera ndi kudzakutenga iwe, iye akutchaja iwe mwakati pa mailosi. Ndipo ngati ndi mlimi, kuchulukitsa kanaini pa teni, akamutulutsira thirakitale yakeyo, izo zimakhala zoipitsitsa kuposa zimenezo.

60 Iwe umayenera kulipira chirichonse chimene iwe wapangiridwa. Chirichonse chimakhala “Kulipira! Ndalama! Kulipira! Ndalama!”

61 Ndipo komabe ndi dzenje lalitali bwanji limene tchimo lakuponyanimo inu! Ndi ndani akanakhoza nkomwe kukutulutsanimu inu mu dzenje la tchimo? Koma Mulungu amakutulutsanimu inu mu dzenje la tchimo, opanda ndalama, opanda mtengo, pamene panalibepo wina aliynense akanakutulutsanimu inu.

⁶² Ngati inu simulipira mochuluka kwa galimoto yokukokaniyo, inu mukhalabe mu dzenjelo. Inu mukuyenera mukhale ndi ndalama kapena inu mukhalabe mu dzenjelo.

⁶³ Koma dzenje loipitsitsa limene inu munayamba mwagweramo, ndi limene mdierekezi anakuponyeranimu inu, dzenje la tchimo ndi kusakhulupirira. Mulungu mwachifuniro adzakutulutsanimu inu, opanda ndalama, opanda mtengo. Ndipo komabe inu mwangogona mu dzenje, mukungosambira mu tchimo, ndipo simukuitanira nkomwe pa Iye.

⁶⁴ Pamene inu mupeza galimoto yokukokaniyo, kawirikawiri iwo amaika tcheni chachikulu kulowa mdzenjelo, amachikulunga icho mozungulira bampala kapena zina zotero, ndi kuyamba kugwejemula. Ndipo mphamvu ya galimotoyo imayamba kukoka, ndipo injini zimayamba kugwira ntchito, ndi kukukokerani inu panja.

⁶⁵ Pamene Mulungu akupezani inu mu dzenje la tchimo, ndipo nakumvani inu mukuitanira pa Iye, Iye amatumiza tcheni chimene chinakulungidwa mozungulira Kalvare, chikondi cha Mulungu, ndipo amadzachikoletsa Icho pa mtima wanu, ndipo amadzaika Mphamvu ya Mzimu Woyera kumeneko, kuti iyambe kukoka. Ndipo izo simulipira kalikonse. Ndipo komabe ife timagona mu dzenje chifukwa ife sitingathe kulipira izo ndi matumba athu. Ife Achimerika timaganiza kuti ife tikhoza kulipira izo kuchokera m'matumba mwathu, koma inu simungathe. Ndi zopanda ndalama kapena zopanda mtengo. Inu simulipira izo ku tchalitchi. Yesu analipira izo pa Kalvare. Koma anthu akuchita manyazi ndi Izo. Iwo akufuna Izo mwanjira yawo yawo. Mulungu ali nayo njira yoti inu mulandirire Izo, ndipo Izo ndi zaulere ngati inu mungazitenge Izo.

⁶⁶ Kawirikawiri, pamene iwo akukoka iwe mu dzenje, iwe umakhala utakandikandika, iwe umayenera kupita, ku chipatala. Ndipo iwo asanayambe kugwira ntchito pa iwe, chinthu chimodzi chisanachitike, iwo amafunsa, “Kodi ati apereke bilu ndi ndani? Ngati ife titi tisoke mabalawa, ngati ife titi timuthire mafutawa, ndi kumubaya kuti—kuti tikubaye iwe katemera wa chiphe cha magazi, kodi iwe uli ndi inshuransi ya mtundu wanjji?” Iwo asanachite chinthu chimodzi, payenera pakhale ndalama pa mzere.

⁶⁷ Koma pamene Ambuye wathu aika tcheni chake cha chikondi mozungulira mtima wako, ndi kukukoka iwe kuchokera mu dzenje la tchimo, Iye amachiritsa mtima wosweka uliwonse, amachotsamo tchimo lonse. Ndipo biluyo imakaikidwa mu nyanja ya kuiwala, kuti asadzakumbukirenso nkomwe za iwe. “Bwerani, opanda ndalama kapena opanda mtengo.” Ziribe kanthu kuti iwe wachekedwa moyipa chotani, ndipo wavulazidwa moyipa bwanji, mmene banja lako lachitira, kapena zimene iwe wachita, palibe bilu kwa izo. Iye amachiritsa

kupweteka kwa mtima konse, amachotsa zisoni zako zonse. “Iye anavulazidwa chifukwa cha mphulupulu zathu, anatunduzidwa chifukwa cha kusaeruzika kwathu; chilango cha mtendere wathu chinali pa Iye; ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Zonsezo ndi zaulere.

⁶⁸ Ndipo ife sitilandira Izo, ndi chifukwa chakuti ife tikulamulidwa ndi mzimu woipa. Ife tikulamulidwa ndi mzimu wa fuko, mzimu wa dziko lapansi, mmalo moti tizilamulidwa ndi Mzimu wa Mulungu, Mzimu Woyera, umene umatitsogolera ife ndi kutilondolera ife ku Zoonadi zonse, ndi kulipangitsa Baibulo kutero.

⁶⁹ Nthawiina m’mbuyomo, ine ndinali kuyankhula ndi wachikunja. Iye anati, “Taganizani za ichi, Bambo Branham. Zosautsa zonse izi za moyo, ndipo chinthu chokhacho chimene ife tiri nacho, chimene ife tinapuluma nacho, ndi zolembedwa zina za Chiyuda zachikale.”

⁷⁰ “Oh,” ine ndinati, “bwana, zimenezo zikhoza kukhala zonse zimene inu muli nazo, koma ine ndiri nacho china choposa zimenezo. Ine ndiri ndi Mzimu wa Iye amene analemba Izo, zimene zimatsimikizira Izo ndi kuzipanga Izo kukhala chomwecho, lonjezo lirilonse.” Iye sanadziwe mmene iye akanati azitengere izo.

⁷¹ Mukuona, inu mukuyenera mubwere ndipo mudzagule opanda ndalama, mudzagule opanda mtengo. Izo sizikutengerani inu kalikonse. Izo ndi zaulere kwa “aliyense yemwe akufuna, muloleni iye abwere.” Mulungu akukukokani inu kuchokera mu dzenje.

⁷² Monga munthu uja pa chipata chotchedwa Chokongola. Iye anali ataponyedwamo, kuchokera m’mimba ya amayi ake, ndi mdierেকেzi yemwe anamulumalitsa iye kumapazi ake. Njira yake yopezera zinthu inali kupempha zithandizo kwa anthu omwe amadutsa. Ndipo pamene iye anakhala pa chipata mmawa umenewo, iye anawona alaliki awiri achipentekosite akubwera. Analibe khobiri limodzi pakati pawo, pakuti iye anati, “Siliva ine ndiribe.” Ndipo khobiri ndi kachidutsa kakang’ono kwambiri ka siliva. “Siliva ndi golidi ine ndiribe.”

⁷³ Ine ndikuganiza munthuyo anaganiza chinachake chonga ichi. “Palibe chifukwa chonyamulira chikho changa.” Mwinamwake iye anali kuyesetsa kuti asunge ndalama zokwanira. Iye anali usinkhu wa zaka forte zakubadwa, ndipo mwinamwake iye amayesetsa kuti asunge ndalama zokwanira, a dokotala akanakhoza kumupangira iye zochirikiza ziwiri, kuti iye aziyenderapo, pakuti, iye, mu mfundo za kumapazi kwake ndi mmene iye anafowoketsedwamo. Ndipo mwinamwake iye ankayenera kuti akhale ndi ndalama, kuti akhale pa mzere, madokotala asanamupatse iye chithandizo. Ndipo ndithudi panalibe chifukwa choti iye azigwirabe chikho chake kwa alaliki

achipentekosite awa omwe analibe kalikonse. Mwayi, iwo a . . . anali osauka kwambiri, sakanapeza nkomwe khobiri kuchokera kwa anyamata amenewo.

⁷⁴ Koma pamene iye anayang'ana mu nkhope zawo! Mmodzi, wamng'ono ndi wamanyazi ndi ubwana; mmodzi winayo, wokalamba ndi wamakwinya; pamene Yohane . . . pamene Petro ndi Yohane amapita ku chipata. Iye anawona chinachake mwa mwamuna wachichepereyo. Ndicho, kuchita manyaziko kunali kopambana pang'ono kuposa kwa wamba. Iye anawona pansi pa makwinyawo ndi nkhawa, za dzuwa la Chigalileya limene linali litawotcha nkhope ya nsodzi wokalambayo, pamene pano panali “chimwemwe chosaneneka, ndi ulemelero wozadza.” Iye anawona chinachake chimene chinawoneka chosiyanyirirapo pang'ono.

⁷⁵ Inu mukudziwa, pali chinachake ndi Chikhristu, chimene chimawapangitsa anthu kuwoneka mosiyana. Iwo ndi anthu okongoletsetsa mu dziko lonse.

Ndipo iye anatenga chikho chake ndipo anangochigwiritsitsa icho.

⁷⁶ Ndipo mtumwi Petro, pokhala wamkulu kwambiri, anati, “Siliva ndi golide ine ndiribe.” Mwakulankhula kwina, “Ine sindingakuthandize iwe chirichonse, kuti ukagulire ndodo zoyendera izi. Siliva ndi golide ine ndiribe, koma chimene ine ndiri nacho!” Iye anali atapita kukagula kwa Iye amene anali ndi uchi ndi zimwemwe za vinyo wa chipulumutso. Iye anali atangobwera, masiku awiri kapena atatu izo zisanachitike, kuchokera ku Pentekosite, kumene chinachake chinali chitachitika.

⁷⁷ Ndipo mnyamatayo analumpha ndi “ameni” wamkulu kwambiri ndi izo, ndipo anayang'ana pa nkhope yake.

⁷⁸ Chinachitika ndi chiyani? Unyolo uja wa chisoni, chifundo cha Iye amene anati, “Ine ndinali ndi chifundo pa odwala,” Mzimu womwe uja unali utatenga malo mu mtima mwa nsodzi wakaleyo. Iye anati, “Ngati ziri za ndalama, ine ndiribe iliyonse, koma ine ndiri ndi chinachake chimene chiti chitenge malo ake kamillionsi. Chomwe ine ndiri nacho!”

⁷⁹ Tsopano kumbukirani, Petro anali Myuda, ndipo iwo amakonda ndalama, mwachirengedwe, koma Myuda uyu anali atatembenuka. Osati, “Chomwe ine ndiri nacho, ine ndikugulitsa iwe.”

⁸⁰ Koma, “Chomwe ine ndiri nacho, ine ndikukupatsa iwe! Chomwe ine ndiri nacho! Ine ndiribe khobiri mthumba mwanga. Ine sindingathe kugula lofu ya buledi. Ine sindingathe kugula chirichonse. Ine ndiribe senti. Koma ngati iwe ungalandire izi, chomwe ine ndiri nacho, ine ndipereka kwa iwe chifukwa icho chinapatsidwa kwa ine.” Ndicho chimene ife tikusowa. “Chomwe ine ndiri nacho, ine ndikukupatsa iwe.”

“Kodi muli ndi chiyani, bwana?”

⁸¹ “Ine ndinali uko kwa Iye amene amagulitsa mkaka ndi uchi, opanda mtengo. Ine ndipereka Izo kwa iwe. Iwe ulibe choti undipatse ine pa Izo. Ngati iwe ungalandire Izo, ine ndikupatsa iwe Izo. Osati ngati wina amene angaikapo mtengo, koma iwo amene angapereke.”

⁸² Chifukwa, “Monga mwaulere mmene inu mwalandirira, mwaulere perekani.” Iko kunali kutuma kwa Ambuye wake, basi masiku atatu chabe apitawo. “Pitani mu dziko lonse, mukalalikire Uthenga. Iye amene akhulupirira ndipo nabatizidwa adzapulumutsidwa; ndipo iye amene sakhulupirira adzawonongedwa. Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira: Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda; iwo adzayankhula ndi malirime atsopano; ngati iwo adzamwa zinthu zakupha, izo sizidzawapweteka iwo; ngati iwo adzatenga njoka, iyo siidzawavulaza iwo. Monga mwaulere mwalandirira, mwaulere perekani.” Myuda ameneyo anali atasinthidwa. [M’bale Branham akugogoda paguwa kanai—Mkonzi.]

⁸³ Chimene ife tikusowa mu Amerika ndi kusinthika, kwa Mzimu Woyera kuti utenge malo a timiyambo tathu tina ta chipembedzo. “Monga mwaulere inu munalandirira, mwaulere perekani.”

⁸⁴ “Chomwe ine ndiri nacho, ine ndikukupatsa iwe: Mu Dzina la Yesu Khristu wa ku Nazareti, dzuka ndipo uyende”; chikhulupiriro mu Dzina losaipitsidwa la Mlengi lija! Nzosadabwitsa iye anapita akutsimphina ndi kulumpha, ndipo akutamanda Mulungu!

⁸⁵ Oh, inu mukudziwa zinthu zazikulu, iye mwinamwake anali atakhala pamenepo zaka forte, akuyesera kuti apeze ndalama zokwanira kuti adzigulire ndodo zinazake, koma iye samatha kuchita zimenezo. Koma pomwepo pa malo osayembekezeka kwambiri, ndi nthawi yosayembekezeka, ndi anthu osayembekezeka, osakwanira, iye anapeza chimene iye ankachifuna. Ndine wokondwa kuti Mulungu amachita izo mwanjira imeneyo.

⁸⁶ Ndipo kagulu ka apang’ono, otchedwa-odzigudubuza usiku wina, ine ndinapeza chimene ine ndinkachifuna, ndalama imeneyo siikanakhoza kugula. Mu gulu la osazindikira, osaphunzira, anthu ovala mwaumphawi, Akuda, kuyamba ndi kuyamba, kunja uko mmalo ochezeramo otembenuzidwa aang’ono, pansu, ine ndinadzapeza mtengo, ngale; pamene wakuda wokalamba uja anadzayang’ana mmaso mwanga, ndipo anati, “Kodi iwe unalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni?” Oh, Ichi chinali chinachake chimene ine ndinkachifuna. Ine sindinkayembekeza kuti ndikanachipeza Icho pakati pa anthu amenewo, koma iwo anali nacho chimene ine ndinkachisowa.

⁸⁷ A U.N. lero, iwo sangavomereze chimene ife tiri nacho, koma ndi chomwe iwo akuchisowa. Khrushchev, ena onse a iwo, akusowa Khristu, mu ubatizo wa Mzimu Woyera. Iwo usintha zikhaliidwe zawo. Iwo uwapanga amuna, omwe iwo amawada, kukhala abale. Iwo uchotsapo dyera, ndi nkhwidzi ndi mikangano; ndipo uyikamo chikondi ndi chimwemwe, ndi mtendere, ubwino ndi chifundo.

⁸⁸ Inde, mmalo osayembekezeka, nthawizina iwe umapezamo chimene iwe umachifuna.

⁸⁹ Kodi ana a Israeli akanapereka chiyani (zofunkha zonse za ku Igupto) pamene milomo yawo inkaukha magazi, pamene lirime lawo limalendewera mkamwa mwawo? Iwo akanatha kupereka golide yense amene iwo anawalanda Aigupto, chifukwa cha kumwa kumodzi kwa madzi abwino ozizira. Atsogoleri awo a mchipululu anali atawatsogolera iwo kuchokera ku thamanda kupita ku thamanda, kuchokera ku maenje kupita ku akasupe, koma monsemo munali mutawuma.

⁹⁰ Kenako apo panabwera, opanda ndalama kapena opanda mtengo! Liwu linayankhula kwa mneneri ndipo linati, “Yankhula kwa thanthwe,” chinthu choumitsitsa mu chipululu, chinthu chakutali kwambiri ndi madzi. Pamenepo ludzu lawo linathetsedwa, opanda ndalama kapena opanda mtengo. “Yankhula kwa thanthwe.” Osati ulipire kwa thanthwelo, koma “uyankhule kwa thanthwelo.”

⁹¹ Iye akanalibe Thanthwe usikuuno. Iye ndi Thanthwe mu dziko lotopetsa. Ngati inu mukuyenda mu dziko lotopetsa limenelo, yankhulani kwa Thanthwe. Simukusowa kumulipira Iye; yankhulani kwa Iye. Ndipo Iye ndi thandizo lopezekeratu mu nthawi ya mavuto. Ngati inu mukudwala, yankhulani kwa Thanthwe. Ngati inu mukudwala ndi-tchimo, yankhulani kwa Thanthwe. Ngati inu mwalema, yankhulani kwa Thanthwe.

⁹² Mukuona, zimaoneka ngati izo zikhala paliponse... Izo zimawoneka ngati, ngati kunalibe madzi kumusi ku malo ochepa amene kunali akasupe, sikukanakhala madzi pamwamba pa phiri ilo, mmphepete mwa thanthwe. Mulungu amachita zinthu mobwerera mmbuyo basi kwa zomwe munthu akuganiza. Thanthwe, malo owumitsitsa mu chipululu, koma Iye anati, “Yankhula kwa Thanthwe.”

⁹³ Lero, anthu anyengedwa kwambiri. Iwo amaganiza ngati iwo angapite ndi kukanena mapemphero awo, kukumulipira wansembe wina kuti anene mapemphero angapo a iwo, kulipira njira yawo kuti adutse. Ngati iwo angamange tchalitchi china chachikulu kwinakwake, ndipo munthu wina wolempera nathandizira icho, kumapitirira kumakhala mu chisiliro, kukhala ndi winawakenso woti azimupempherera iye, iye amaganiza kuti ndi zimenezo. Mulungu samafuna ndalama zanu zonyansa. [M’bale Branham akugogoda pa guwa

katatu—Mkonzi.] Chinthu chonse chimene Iye akuchifuna ndi kudzipereka kwanu ndi moyo wanu kuti uziyankhula kwa Iye. Mulungu wakupatsani inu ndalama, inu musawonongere izo pa zinthu zimene sizikhutitsa. Muziwonongere izo pa zinthu zimene zimakhutitsa. Koma kubweretsa kukhutitsidwa kwenikweni, inu simungakupeze iko kufikira inu mutayankhula kwa Thanthwe.

⁹⁴ Iye anabweretsa madzi-opereka moyo, opanda ndalama kapena opanda mtengo. Ndipo iwo anamwa, ndipo ngamila zawo zinamwa, ndipo ana awo anamwa, ndipo anakhalabe kasupe akuyenderera mu chipululu.

⁹⁵ Ndipo chomwechonso Iye ndi Thanthwelo lero, mu dziko lotopetsa ili, kwa anthu amene akuwonongeka. “Aliyense amene akhulupirira pa Iye sadzawonongeka, koma adzakhala nawo Moyo Wamuyaya.”

⁹⁶ Zindikirani. Usiku uliwonse, iwo sankasowa kuti azisinkhasinkha za mkate. Mkate wawo umabweretsedwa kwa iwo, usiku uliwonse, watsopano.

⁹⁷ Iye timapita lero kukagula lofu ya buledi. Ngati iwe uli wopemphetsa, ndipo iwe ukapita ku sitolo uko, ndi kukati, “Ine ndikufuna lofu ya buledi.”

⁹⁸ Iye akhoza kunena kuti, “Ndiwonetse ine, kaye poyamba, ndalama yako. Ine ndikuyenera ndikhale ndi ma senti twente-faifi pa lofu ya buledi iyi.”

⁹⁹ Ndipo inu mumapeza chiyani mukagula iyo? Ichi ndi chakumbali pang’ono, koma inu mumapeza chotsikitsitsa chimene tirigu angapange. Iwo amachotsamo ma—mavitamini onse mwa iye, deya yense, ndi kumupereka iye kwa nkumba. Amasakaniza ka mulu ka zomata komwe kamamata deyayo pamodzi, ndipo amamusefa iye, ndi kupanga lofu ya buledi, wopangidwa ndi manja auye, awutchisi, nthawi zambiri. Inu mukuona zimene inu mumazipeza mu buledi wanu, nthawizina, mibulu ya tsitsi, ndi zinthu zachiwerewere, ndi tizidutswa tokulungira, ndi china chirichonsecho chimene chimagwera mophikira mmenemo. Anthu ochimwa okhala ndi matenda opatsirana pogonana, ndi chirichonse, kuzisakaniza mmenemo. Ngati inu mutawona iye akupangidwa, inu simungathe nkomwe kumudya iye. Ndipo, komabe, inu mumalipira masenti twente-faifi anu kapena inu simumupeza iye.

¹⁰⁰ Ndipo Mulungu amawadyetsa iwo usiku uliwonse, ndi mkate wopangidwa ndi manja a Angelo; opanda ndalama, opanda mtengo. Ndipo, lero, mkate umenewo ukuimira Khristu, Moyo wauzimu, anatsika kuchokera Kumwamba, kuti adzapereke Moyo Wake.

¹⁰¹ Ndipo Mulungu amawapatsa ana Ake, tsiku ndi tsiku, chowachitikira chatsopano. Inu mukukumbukira, ngati iwo awusunga mkatewo, iwo umawonongeka.

¹⁰² Inu mumamva wina akuyankhula zakuti, “Chabwino, ine ndiri. . .Ine ndikuuzani inu. Ndine wa Chilutera. Ndine wa Chipresibateria, Baptisti. Ndine wa Chipentekosite,” imeneyo ndi lofu ya buledi chabe yopangidwa ndi dzanja la munthu. Ndizo zonse zomwe ziriko kwa izo, zonyansa basi, ndi zopangidwa ndi manja a anthu.

¹⁰³ Koma pamene iwe umva chokuchitikira cha umboni, watsopano, “Mmawa uno, mu pemphero, Mzimu Woyera unabatiza moyo wanga mwatsopano,” oh, m’bale, chimenecho ndi Chakudya cha Angelo. Iye amawadyetsa iwo mwatsopano, tsiku ndi tsiku, kuchokera Kumwamba.

Mivumbi ya madalitso ife tikuifuna.
Madontho a chifundo motizungulira ife
akugwa,
Koma pa mivumbi ife tikuchonderera.

¹⁰⁴ Oh, inde, tumizani kuchokera Kumwamba, yatsopano, Ambuye, Khristu Mkate wa Moyo. Muwuponyere Iwo mu mtima mwanga, ndipo mundilole ine ndikondwerere Kukhalapo Kwake kwakukulu.

¹⁰⁵ Ndithudi, iwo anali othokoza. Iwo anali oyamikira. Ndipo mwamuna aliyense kapena mkazi amene wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu, ndi kulandira Mzimu Woyera, nthawizonse adzakhala wothokoza. Ziribe kanthu kuchitika chiyani, inu mudzakhala oyamikira.

¹⁰⁶ Monga mnyamata wamng’ono, wakhungu uko ku mapiri, Benny wamng’ono, iye anabadwa. Pafupifupi usinkhu wa miyezi eyiti yakubadwa, ng’ala inayamba kumayala mmaso mwake. Makolo ake anali osauka. Iwo amakhala mmbali mwa phiri la makande. Ndipo iwo ankadziwa kuti ma opareshoni amenewo akanakhoza kupulumutsa maso a Benny wamng’onoyo, kuti azikhoza kupenya. Iye anali mnyamata tsopano wa pafupifupi usinkhu wa zaka thwelofu zakubadwa. Makolo ake amangokwanitsa zokwanira zopezera buledi ndi nyama pa chaka. Iwo sakanakwanitsa opareshoniyo.

¹⁰⁷ Oyandikana nawo onse, pamodzi, amamuwona Benny wamng’ono akumayesera kusewera ndi tiana tating’ono kunja uko, wakhungu. Iye samatha kuwona zimene iye amachita. Iwo amamva naye chisoni. Ndipo mmodzi aliyense, chaka chimenecho, anaikamo kagawo kakang’ono kowonjezera ka mbewu. Iwo anagwira ntchito molimbikirapo pang’ono mu dzuwa. Ndipo pamene mbewu zinagulitsidwa mu chilimwe, iwo anatenga ndalamazo ndipo anamuika Benny wamng’ono pa sitima, ndi kumutumiza iye kwa adokotala.

¹⁰⁸ Iwo anachita opareshoniyo ndipo inayenda bwino. Ndipo pamene iye ankabwererako, oyandikana nawo onse anasonkhana pamenepo pamene Benny wamng’ono amatsika

sitima. Maso ake aang'ono owala, akunyezimira. Iye anayamba kufuula ndi kulira, pamene iye amayang'ana pa nkhope zawo.

¹⁰⁹ Mmodzi wa makondakitarawo anati, “Mwana, zinakutengera ndalama zingati oparesoni imeneyo?”

¹¹⁰ Iye anati, “Bambo, ine sindikudziwa zomwe zawatengera anthu awa. Koma ndine wokondwa kuti ine ndikutha kuwona nkhope zawo, omwe analipira mtengo wake.”

¹¹¹ Umo ndi mmene ife timamverera. Ine sindikudziwa chomwe Izo chinamutengera Mulungu. Ine ndikudziwa Iye anandipatsa ine chopambana chomwe Iye anali nacho, Mwana Wake. Koma ndine wothokoza kwambiri kukhala ndi kupenya kwauzimu uku, kuti ine ndikutha kupenya mu nkhope Yake ndi kudziwa kuti Iye anandifera ine. Ine sindikudziwa zomwe Izo zinamutengera Iye. Ife tiribe njira yoti nkuziwerengera izo. Mtengowo unali waukulu kwambiri. Ine sindingathe kukuuzani inu momwe iwo unaliri. Koma ndine wothokoza. Ndine woyamikira, kuti, m'menemo ine ndinali wakhungu nthawiina, ine tsopano ndikutha kupenya.

¹¹² Ndine woyamikira kuti pamene a Mayo Brothers anandiuza ine kuti nthawi yanga yatha, pamene madokotala anandiuza ine kuti ine sindingathenso kukhala moyo, zaka twente-faifi zapitazo, ine ndiri moyo lero. Ine sindikudziwa zomwe zinamutengera Mulungu, koma ndine wothokoza kuti ine ndiri moyo.

¹¹³ Nthawiina ine ndinali wochimwa, womangidwa mu tchimo, ndi kupweteka kwa mtima, kumawopa imfa. Koma, lero, imfa ndi chigonjetso changa. Alaluya! Iyo ikhoza kokha kundibweretsa ine mu Kukhalapo kwa Iye yemwe ine ndimamukonda, kuti ine nditha kuyang'ana pa nkhope Yake. Iye anasintha chinthucho, ndi oparesoni, Iye anatenga mtima wanga ndipo anawupanga iwo kukhala watsopano. Ine ndikudziwa chinachake chinachitika kwa ine.

¹¹⁴ Mu pepala kugwa kwa masamba kwapitaku, mu Minnesota, kumeneko kunali mnyamata wamng'ono yemwe anatenga njinga yake ndi kupita ku tchalitchi mmawa wina, ku Sande sukulu. Mwamuna wamng'ono wina mwa oyandikana nawo, iye analibe chochita ndi Sande sukulu, iye anamutenga bwenzi wake wamkazi ndipo anapita kumakasewera pa ayezi. Ndipo bamboyo anali munthu wachikulire, ndipo iye anafika pa ayezi wopyapyalayo ndipo anagwapo. Iye anali atamuseka mnyamata wamng'onoyo mmawa uja pamene iye amayenda mu msewu, anamuza bwenzi wake wa mkazi, anati, “Ndi kagulu ka otentheka ako kakupita ku tchalitchi icho.” Ndipo pamene iye anagwa pa ayezi, bwenzi lake la mkazi anali kutali ndi iye. Iye anali wo pepuka; iye anadutsapo. Koma pamene iye anabwera ndi kudzaika mikono yake pa ayezi, iye anawumapo, ndipo anatsakamira pa ayeziyo.

¹¹⁵ Bwenzi wake wa mkazi anayesera kuti amugwire iye, koma iye anali wolemERA kwambiri, mkaziyo amaswa ayeziyo. Iye anamufuulira iye, “Bwerera! Bwerera! Iwe ugwera mkati, ndipo ife awiri tonse timira.” Iye anafuula, iye analira, ndipo panalibe choti nkumuthandiza iye.

¹¹⁶ Patapita kanthawi, uko pamwamba pa phiri, panabwera kanjinga kakang’ono, kakupalasa, mnyamata wamng’ono ali ndi Baibulo mkhwapa mwake. Iye anamva mifuuyo, ndipo iye anathamangitsa njinga yake yaing’ono. Analiyika Baibulo lake pansi, ndipo anathamangirako pa ayezi. Anakwawa pamimba yake yaying’ono, atavala zovala zake zabwino, mpaka anagwira mikono ya bamboyo, ndipo anapitirira kumukokera iye m’mbuyo, kufikira iye anamutulutsamo iye mu ayezimo. Anathamangira uko ndi kukaimitsa galimoto. Iwo anaitanitsa ambulasi ndipo anamutengera iye ku chipatala.

¹¹⁷ Iye atatha kupita ndi kukalipira ambulasi, anawalipira madokotala chifukwa cha majekeseni a chibayo ndi zinthu zimene iye ayenera kuti anampatsa, iye anabwera kwa mnyamata wamng’ono. Iye anati, “Mwana wanga, kodi ine ndiri ndi zako zingati?”

Iye anati, “Palibe.”

¹¹⁸ Iye anati, “Ine ndiri nawe ngongole ya moyo wanga.” Taganizani za zimenezo. Ndalama sizikanatha kulipira izo. Unali moyo wake.

¹¹⁹ Umo ndi mmene ife tikuyenera kumamvererera kwa Mulungu. Osati kuti tigule njira yathu ndi chinachake; koma ife tiri naye ngongole Mulungu ya moyo wathu, pakuti ife tinali kufa ndipo tinkamira mu dzenje la tchimo. Mulungu anaponyera mikono Yake ndi mwinjiro pa ine.

Ine ndinali kumira mozama mu tchimo,
Kutali ndi gombe la mtendere,
Nditadetsedwa mwakuya kwambiri mkatimu,
Kumira koti sindidzadzukanso;
Koma Mbuye wa mnyanja
Anamva kulira kwanga kosimidwa,
Kuchokera mmadzi ananditukula ine,
Tsopano ndine wotetezeka.

¹²⁰ Ine ndiri naye Iye ngongole ya moyo wanga. Inu muli naye Iye ngongole ya moyo wanu. Inu muli naye Iye ngongole ya moyo wanu, kuti muzimutumikira Iye; osati kuupereka iwo, kumayendayenda ndi kumadzibwekerera za chipembedzo chanu cha tchalitchi; osati kumayendayenda ndi kumawatsutsa ena; koma kuyesera kuti muzitumikira ndi kuwapulumutsa ena, ndi kuwabweretsa iwo ku chidziwitso cha Ambuye Yesu Khristu.

¹²¹ Mwana wolowelera. Potseka, ine ndikhoza kunena ichi. Pamene iye anali atawononga chuma chake chonse, chuma cha abambo ake, ndi kukhala kwa chisokonezo, ndipo pamene iye

amabwerera kwawo. . .Iye amagona mu khola la nkumba, ndipo iye anabwera pozizindikira yekha. Ndipo iye anati, “Ndi antchito angati olembedwa, abambo anga alinawo, amene alinazo zochuluka zosunga, ndipo ndine pano ndikufa, chifukwa chosowa.” Bwanji ngati iye akanayesera kunena kuti, “Ndikudabwa ngati ine ndiri ndi ndalama zina zomwe ine ndingathe kukawabwezera abambo (zomwe ine ndinawononga pothawa) ndi izo?” Koma iye amadziwa chikhalidwe cha abambo ake, ndipo iye anati, “ine ndidzuka ndipo ndipita kwa abambo anga.”

¹²² Abambowo sanati, “Dikira miniti, mwana! Kodi iwe ukudzabweza ndalama zanga?” Ayi. Iye sanamuwerengere iye machimo ake. Iye anali wokondwa kuti iye amabwerera. Iye anali wokondwa kuti iye wafika podzizindikira yekha, chifukwa iye anali mwana wake. Iye anali mwana wake yemwe. Iye anali wokondwa kuti iye anali pa njira yake ya kwawo. Tsopano, iye sanavomereze tchimo lake, koma iye anali wokondwa pamene iye anabwera podzizindikira yekha ndipo anati, “ine ndachimwa pamaso pa Mulungu wanga, ndi pamaso pa abambo anga. Ine ndidzuka ndipo ndipita kwa iwo.”

¹²³ Ndipo pamene iwo anamuwona iye, patali, iwo anathamangira kwa iye ndipo anamupsyopyona iye. Ndipo iwo anati, “Muphe mwana wang’ombe wonenepayo,” opanda ndalama. “Mundibweretsere mwinjiro wapamwamba kwambiri,” opanda ndalama. “Mundibweretsere mphete,” opanda ndalama, “muiveke iyo pa chala chake. Tiyeni ife tidye, timwe, ndipo tikondwere, pakuti mwana wanga uyu anatayika ndipo tsopano wapezeka. Iye anali wakufa, ndipo tsopano iye ali ndi moyo kachiwiri. Tiyeni ife tikondwerere izo.”

¹²⁴ Ndinene ichi abwenzi, kuti nditseke. Chinthu chokhacho chimene chimakhutitsa, zinthu zenizeni zokhazo zomwe ziripo, zinthu zabwino zokhazo zomwe ziripo, sizingathe kugulidwa ndi ndalama. Izo ndi mphatso zaulere za Mulungu, mwa Yesu Khristu: chipulumutso cha moyo; chimwemwe. Bwerani ndipo mudzadye, ndipo mudzakhutitsidwa.

Chifukwa chiyani inu mukuwonongera ndalama pa izo zimene siziri chakudya? ndikugwirira ntchito yanu pa izo zimene sizimakhutitsa? mverani mochimika kwa ine, ndipo mudzadye. . .izo zimene ziri zabwino, ndipo mulole mtima wanu ukondwere wokha mu kunenepa uko.

Tcherani makutu anu, ndipo mubwere kwa ine: imvani, ndipo solo yanu idzakhala moyo; ndipo ine ndidzapanga pangano losatha ndi inu, ngakhale zifundo zokhazikika za Davide.

¹²⁵ Zinthu zonse zomwe ziri zokhalitsa, zinthu zonse zomwe ziri zabwino, zinthu zonse zomwe ziri zokondweretsa, zinthu

zonse zomwe ziri Zamuyaya, ndi zaulere, ndipo simulipira chirichonse. Kumapeto a kulemba kwa Bukhu ili, Ilo linati, “Aliyense amene akufuna, muloleni iye abwere ndipo adzamwe kuchokera ku Madzi a kasupe a Moyo, kwaulere,” opanda ndalama, opanda mtengo. Chifukwa chiyani inu mumawononga ndalama pa izo zomwe sizikhutitsa, ndi kulola zinthu zenizeni zimene zimakhutitsa, zaulere, zipite zosasamalidwa ndi inu? ”

Tiyeni ife tipemphere.

¹²⁶ Pamene inu muli chete ndi mu pemphero, kodi alipo, mu chipinda chino, mmawa uno, iwo amene sakumwa kuchokera ku Kasupe ameneyo, amene zokhumba za dziko zikanalibe m’moyo mwanu, ndipo inu mukufuna musinthe malo anu omwerapo, mmawa uno, kapena katapira wa ndalama zanu? Inu mukufuna kuti mubwere ndi kudzagula kuchokera kwa Mulungu, (opanda ndalama, opanda mtengo), uchi ndi mkaka, zimwenwe za vinyo? Kodi mungakweze m’mwamba dzanja lanu, ndikuti, “Mundikumbukire ine, M’bale Branham, pamene inu mukupemphera”? Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Alipo ena omwe angati, “Ndikumbukireni ine, M’bale Branham, pamene inu mukupemphera”?

¹²⁷ Ena a inu anyamata, eya, amene mwaononga moyo wanu. Ma—ma—ma ora amene amayi anakhala mu pemphero chifukwa cha inu, ndi abambo, kuphunzitsa konse kumene kunachitika pa inu, ndipo komabe inu mwazitaira izo kumbali, kuti muzimvetsera ku kunong’oneza kwa mdierেকে. Tsopano inu mukukhumba nyimbo za mdziko, zinthu za mdziko. Ndipo inu mukubwera podzizindikira nokha, monga wolowererayo mu khola la nkumba. Kodi inu mungakweze dzanja lanu, mlongo, m’bale, ndikuti, “Mulungu, ndikumbukireni ine. Ndibweretseni ine kwa inemwini, mmawa uno, mundilore ine ndibwere ku nyumba ya Atate anga”? Izo sizikutengerani inu chinthu chimodzi. Iye akuyembekezera inu. Ziribe kanthu zimene inu mwachita, “Ngakhale machimo anu akhale ngati kapezi, iwo adzayera ngati matalala; ofiira ngati magari, iwo adzayera ngati ubweya wankhosa.” Kodi iwo ali mu Kupezeka kwa Umulungu, amene angakweze dzanja lawo?

¹²⁸ Iwo amene akudwala ndi osowa, anene, “ine—ine ndinagwera mu dzenje. Satana wa—wachita choyipa kwa ine. Iye wandilumalitsa ine ndipo wandidwalitsa ine, kapena chinachake. Ine ndikukhumba, mmawa uno, unyolo wa chikhulupiro cha Mulungu kuti usunthire mu mtima mwanga, kuti undikokere m’mwamba ine kundichotsa mu dzenje ili, monga mwamuna wa pa chipata chotchodwa Chokongola.” Kwezani manja anu. Mulungu akudalitseni inu, aliyense.

¹²⁹ Ambuye, ine ndikubweretsa kwa Inu, ora lino, iwo amene akweza manja awo, pa chikhululukiro cha machimo awo.

Inu ndinu Mulungu, ndi Mulungu yekha. Apo pomwe iwo akhala tsopano, ndi pamene Inu mwayankhula ndi iwo. Ndi pamene Inu mwawatsimikizira iwo kuti iwo ndi olakwa, pamene Mawu apeza malo Ake, ndipo Mzimu Woyera unayamba kuyankhula, ndi kunena, “Inu ndi olakwa. Tembenukani, ndipo mubwererense kwa Mulungu Atate.” Ndipo iwo anakweza manja awo, kuwonetsera kuti iwo akufuna atuluke mu khola la nkumba ili la dziko lapansi, kuti abwere ku nyumba ya Atate, kumene kuli zochuluka, kumene iwo sadzasowekera kubweretsa chirichonse. Monga mlakatuli wanena bwino, “Palibe kanthu m’manja mwanga kamene ine ndikubweretsa, mophweka basi ku mtanda wanu ine ndikukangamirako.” Mulole iwo abwere, mokoma, modzichepetsa, ndipo atsutsidwe, ndi kupereka miyoyo yawo. Ndipo Inu mudzawabweretsera mwinjiro wapamwamba; ndi mphete, ndi kuika pa zala zawo; ndi kuwadyetsa iwo ndi Manna a Mwanawankhosa wophedwa. Perekani izi, Ambuye.

¹³⁰ Alipo awo amene akudwala ndi otunduzidwa. Iwo ndi osowa. Satana wawaponyera iwo mu dzenje, nzosakaikitsa, akusowa ndalama za opareshoni. Nzosakaikitsa, mwinamwake, ambiri a iwo sakanakhoza kuchitidwa opareshoni. Mwinamwake adokotala sakanatha kuchotsa choyambitsacho, ngakhale ngati iye akanakhala ndi ndalama zochuluka kwambiri. Koma Inu ndinu Mulungu. Ndipo ine ndikupemphera kuti ora lomwe lino, pansi pa kudzodza kwa Mzimu Woyera komwe kuli pano tsopano, kuti Inu muchiritse aliyense wa iwo. Mulole iwo achiritsidwe, kuchokera ku mutu wawo mpaka ku mapazi kwawo, kachidutswa kalikonse.

¹³¹ Ngati iwo ali opanda chimwemwe; chipulumutso chawo, iwo sakukondwera nacho Icho konse. Monga Davide anati, wakaleyo, “Bwezeretsani chimwemwe cha chipulumutso changa.” Mulole iwo alandire chimwemwe ndi chisangalalo, pa kulunda kwawo ndi kulema, pakuti Inu ndinu Thanthwe mu dziko lotopetsa. Ndinu mthunzi mu nthawi ya mkuntho. Pamene mdierekezi akuvunga nthenda iliyonse ndi mzinga pa iwo, Ndinu pobisalapo mu nthawi ya mkuntho. Mulole izo zikhale chomwecho, lero, Mulungu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

Mofewa ndi mwachikondi Yesu akuitana,
 Akuitana pa inu, ndi ine;
 Ngakhale ife tachimwa, Iye ali ndi chifundo
 ndi chikhululukiro,
 Chikhululukiro pa iwe, ndi ine.

Bwera kwathu . . .

¹³² Tsopano ngati inu mukukhumba kutero, bwerani ku guwa ndipo mudzagwade pansu, ife tikhoza kupemphera nanu,

kukudzodzani inu, chirichonse chimene ife tikhoza kuchita. Ndinu olandiridwa.

. . . wolema, bwerani kwathu;
Moona, mwachikondi, Yesu akuitana,
Akuitana, O wochimwa, bwera kwathu!

¹³³ Kodi inu mukunkonda Iye? Teddy, iwe ungatipatse ife poyambira, “Ine ndinkonda Iye, ine ndinkonda Iye chifukwa Iye anayamba kundikonda ine.” Kodi iwe ungapapeze?

¹³⁴ Tiyezi tiyimbe iyo kwa ulemelero Wake, ife tisanasinthe dongosolo la msonkhano, kamphindi chabe. Uku ndi kupembedza. Uthenga wapita. Ndine wokondwa kwambiri kuti inu mwaulandira Iwo. Mupemphere kuti Iwo ukuchitireni inu zabwino, pakuti iwo wandichitira ine zabwino poyankhula Iwo. Ine ndikupemphera kuti kudzodza komweko kumene kunaperekedwa kwa ine, kuti kuyankhule Iwo kwa inu, inu mwaulandira Iwo mu kudzodza komweko komwe Iwo unatumizidwiramo. Ambuye adalitse Iwo ku mtima kwanu. Chabwino.

Ine ndinkonda Iye,

Tsopano ingotsekani maso anu, pamene ife tikuimba. Kwezani m’mwamba manja athu.

Ine ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

¹³⁵ Tsopano tiyezi tingoweramitsa mitu yathu, tiing’ung’uze iyo. [M’bale Branham akuyamba kung’ung’uza *Ine Ndinkonda Iye*—Mkonzi.] Inu mukunkonda Iye? Kodi Iye siali weniweni mu mtima mwanu? Kodi palibepo chinachake chokhudza Iye, chimene chiri chenicheni basi? Ine ndinkonda Iye chifukwa Iye anayamba kundikonda ine, anaponya chingwe cha Moyo kuchokera ku Kalvare, anadzachikoletsa icho ku mtima wanga.

¹³⁶ Musaiwale, M’bale Kurmmond [Drummond] atilalikira ife usikuuno, usiku wa mgonero. Ngati inu mukuwakonda Ambuye, mubwere kuno ndipo mudzadye mgonero ndi ife. Ambuye akalola, ine ndidzakhala nanu inu kuno. Ameneyo ndi mpongozi wamwamuna wa M’bale Tonny Zabel; M’bale Thom wochokera ku Africa; mwana wake wamwamuna, mnyamata wabwino; wabwino kwenikweni, Mkhristu wokhazikika, mlaliki wabwino wamng’ono.

Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

¹³⁷ Pamene tiri ndi mitu yathu chiweramire tsopano, pamene piyano idzipitirira.

138 Ambuye Yesu, ife tikukonzekera kuti tilowe msonkhano wina, Ambuye. Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha Mzimu Woyera umene wayankhula ku mitima yathu. Ndipo ndife okondwa, Ambuye, kuti Inu mwatichitira ife ichi. Ndipo mulole Mawu Anu asabwerere kwa Inu opanda kanthu, koma mulole Iwo akwaniritse icho chomwe Iwo anakonzedwa kuti adzachite. Mulole Iwo akhale mmitima yathu yonse, kudziwa kuti zinthu zonse zenizeni ndi zinthu zokhalitsa zimachokera kwa Mulungu, opanda ndalama, opanda mtengo. Chifukwa chiyani ndiye ife timavutika ndi zinthu, ndi kuzipanga izo chochitika cha moyo-ndi-imfa chotero, pa zinthu zimene zidzawonongeke? Tiloreni ife tivutikire mochulukwa, Ambuye, pa zinthu zimene sizidzawonongeke, zomwe ziribe mtengo. Mtengo unalipiridwa kwaulere, ndi kuitana molandila, “Aliyense akufuna, Muloleni iye abwere.”

139 Mudalitse gawo lotsatira la msonkhano uno. Perekani izi, Ambuye. Ndipo mukumane nafe usikuuno. Mudalitse msonkhano wa ubatizo. Mulole pakhale kutsanulira kwakukulu. Mulole anthu awa, amene ati abatizidwe mu Dzina la Mwana Wanu wokondedwa, Ambuye Yesu, mulole iwo adzadzidwe ndi Mzimu Woyera. Mulole anthu awa, amene anakweza manja awo, kuti akulapa, mmawa uno, machimo awo, mulole iwo abwere, adzalowe mu zovala za ubatizo, ndi kulowa mu dziwe, ndi kudzatsimikizira kwa dziko lapansi kuti iwo akhululukidwa machimo awo. Ndipo iwo akubatizidwa, kuti iwo achotsedwe mu bukhu. Perekani izi, Ambuye.

140 Mukhale ndi M'bale Drummond usikuuno pamene iye azitibweretsera ife uthenga, watsopano wochokera ku Mpandowachifumu. Mumudzodze iye ndi Mzimu Woyera. Ndipo mukhale nafe pamene ife tizidya mgonero. Mulole mitima yathu ikhale yoyera ndi yangwiro, mulole pasakhale chodetsa chirichonse mwa ife. Mulole Magazi a Yesu atitsuke ife ku tchimo lonse. Perekani izi, Ambuye. Chotsani kudwala pakati pathu, ndipo tipatseni ife chimwemwe ndi mtendere. Kudzera mwa Yesu Khristu ife tikupempha izi. Amenii.

Ine ndinkonda . . .

141 Kodi inu mukunkonda Iye? Tsopano kwezani m'mwamba manja anu kwa Iye.

Ine ndinkonda Iye

Chi-

Tsopano fikirani ndipo mugwirane chanza ndi winawake wapafupi nanu.

. . . poyamba . . .

(Russell, ine ndikunkonda Iye. Ngati ine ndingafe lero, ine ndikunkonda Iye.)

Ndipo anandigulira . . .

Uko nkulondola, fikirani pozungulira ndipo mugwirane chanza.

. . . chipulumutso

Pa Kalvare . . .

Chabwino, M'bale Neville, ndi chonena chake.
Chabwino. 

OPANDA NDALAMA KAPENA OPANDA MTENGO CHA59-0802
(Without Money Or Without Price)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham unalalikidwa mu Chingerezi Lamlungu mmawa, Ogasiti 2, 1959, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A. Unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mu chaka cha ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©2018 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org